

# Njira Zabwino za Pemakacha

Kafukufuku Woyeza Minda/Madimba Ndi Mbewu  
M'Mudzi Wa Khundi

Wolembe: Austin, Juliet, Asa ndi Dikirani

Wotanthauzira: Dikirani

Wothandiza: Vincent Makiyi, Isaac, Dikirani ndi alimi wonse kwa  
Khundi

Mayina ya alimi wokondedwa kuchokera kwa Khundi:

1. A mfumu Chimbiya
2. Isaac
3. Maseko
4. Philimon
5. Denisi
6. Florida
7. Daniel
8. Rosaline
9. Chokani
10. Marita



# Njira Zabwino Za malimidwe Kuchokera Kwa Alimi A Kwa Khundi

1. Ulimi wa kasinthatintha wa mbewu m'munda  
(Crop Rotation)
2. Ulimi wophatikiza mbewu zosiyanasiyana m'munda  
(Intercropping)
3. Kukoza akambewa (mabosi) m'munda  
(Box Ridges)
4. Ulimi wa mibedi yokhazikika m'munda  
(Permanent Beds)
5. Kukoza akalozera m'munda  
(Contours)
6. Ulimi wophimbika nthaka  
(Residues & Mulching)
7. Kupanga compositi manyowa  
(Compost)
8. Kubzala ntchire (udzu) m'munda  
(Vegetation to prevent soil erosion)
9. Ulimi wophatikiza mbewu ndi mitengo m'munda  
(Agroforestry)
10. Ulimi wokhala ndi madimba apakhomo  
(Home Gardens)

Bukuli lalembedwa ndi anthu awa: Austin, Juliet, Asa a kwa Merica ndi Dikirani, m'Malawi.

Bukuli linali m'chingerezi ndipo latanthauziridwa m'Chicheŵa ndi Dikirani kuchokera kwa Khundi.

Fundo zonse zachokera kwa alimi a kwa Khundi.


Kuthokoza: Tikuthokoza alimi a kwa Khundi ndi njira za ulimi zabwinozi.  
Mulungu akudalitseni.

# 1. Kasinthasintha wa mbewu m'munda (Crop Rotation)

Aka ndi kalimidwe kolima mbewu posinthasintha malo m'munda kapena m'dimba. Chitsanzo: Mbali yina ya munda kulima chimanga, yotsalayo mtedza ndipo chaka chobwera, malo achimanga padzalimidwa mtedza pamene potsalapo chimanga.

Ubwino wakasinthasintha wa mbewu m'munda:

- a) Manyowa, chifukwa nyemba/mtedza zimawonjezera chonde m'nthaka.
- b) Matenda ngakhalenso tizirombo zimapewedwa m'munda.




## 2. Kulima mbewu zosiyanasiyana/mophatikizana m'munda (Intercropping)

Aka ndi kalimidwe kolima mbewu zoposera ziwiri zamitundu zosiyana m'munda.

Ubwino wolima mbewu zosiyanasiyana m'munda:

- Mbewu zina sizifuna madzi ambiri, chotero mvula ikachepa mbewuzi zimakhwimabe pamene zina zimawuma/zimafa. Chitsanzo: chinangwa ndi chimanga m'munda, chinangwa chimapirira kuchilala cha mvula.
- Kudalirana kwa mbewu, chimanga ndi nyemba mwachitsanzo: Chimanga chimadalira nyemba chifukwa zimawonjezera chonde m'nthaka pamene nyemba zimadalira chimanga kuti ziyangepo.




### 3. Kukoza akambewa/mabokosi m'munda (Box Ridges)

Aka ndi kalimidwe kokoza/kuyika akambewa mopingasa mizere m'munda.

Ubwino wokoza akambewa m'munda:

- a) Kusunga madzi, chifukwa cha mabokosi, madzi amolowa pansi.
- b) Nthaka siyikokoloka m'munda chifukwa madzi sakhala ndi mphavu.




#### 4. Ulimi wamibedi yokhazikika m'munda (Permanent Beds)

Aka ndi kachitidwe kolima/kukhala ndi mibedi m'munda kwamuyaya.

Ubwino wamibedi m'munda:

- Ntchito imakhala yochepa chifukwa mumangopanga nthawi imodzi yokha basi
- Nthaka sikhala yogwirana zomwe ndizabwino kumizu yambewu kuti izitenga chakudya m'nthaka mosavuto
- Kagwiritsidwe bwino kamalo, chitsanzo malo amizere yitatu pamakozedwa mibedi yiwiri
- Kuteteza kukokoloka kwa nthaka monga m'mibedi yanjoka (yokhotakhota) madzi sathamanga m'mibedi yanjoka




## 5. Kukoza akalozera m'munda (Contours)

Aka ndi kachitidwe kokoza akalozera kapena kuti migula m'munda. Popanga akalozera m'munda A-Frame ndi chida chomwe amagwiritsa ntchito poyesa malo m'munda.

Ubwino wokhala ndi akalozera m'munda:

- Kuteteza kukokoloka kwa nthaka
- Amathandiza kuti nthaka yikhale ndi madzi




## 6. Kuphimbika nthaka (Residues)

Aka ndi kalimidwe koyika mapesi kapena udzu mukhwawa m'munda wamizere pamene wamibedi amayika pamwamba.

Ubwino wophimbika nthaka:

- Nthaka yisakokoloke chifukwa udzu pamwamba pamibedi umachepetsa mphamvu yamadzi
- Udzu ngakhaleso mapesi akawolerana, amakhala manyowa chomwe chili chakudya cha mbewu
- Madzi amalowa bwino m'nthaka






## 7. Kugwiritsa ntchito kompositi manyowa (Compost)

Kompositi manyowa ndi fotetereza walokolo yemwe amapangidwa kuchokera kuzomera kapena ndowe yaziweto. Mlimi amasakaniza ndowe/mapesi/udzu poziwunjika pamodzi ndi kuthirapo madzi. Pa masiku awiri (2 days) aliwonse zinyalala zimayenera kutembenezidwa kamodzi. Pakutha masabata awiri ndi masiku anayi (18 days) manyowa amakhala kuti atheka akhoza kugwira ntchito m'munda/m'dimba. Pakufunika kupanga manyowa mosaposeera milingo khumi ndi yisanu (15 meters) ndi munda kapena dimba chifukwa mutha kunyamula mosavuta kupititsa kumunda/m'dimba.

Ubwino wa kompositi manyowa:

- Udzu/mapesi/ndowe zimapezeka mosavuta kumudzi
- Ndiyosandula komaso ndiyosavuta kupanga
- Kuwonjezera chonde chambiri m'nthaka
- Nyongolotsi zimakula bwino zomwe ndi zofunika m'nthaka chifukwa zimawonjezera chonde, kuti m'nthaka yizipuma




### 8. Kubzala ntchire (udzu) (Vegetation for soil erosion)

Aka ndi kachitidwe kobzala udzu m'munda mmalo wovuta madzi kapena migula. Kubzala vetiva ndi mitengo m'migula.

Ubwino wobzala ntchire (udzu):

- a) Kusunga madzi m'munda
- b) Nthaka sikokoloka chifukwa madzi sathamanga
- c) Mitengo kapena udzu zimawonjezera chonde m'nthaka




## 9. Ulimi wophatikiza mbewu ndi mitengo m'munda (Agroforestry)


Aka ndi kalimidwe kolima mbewu ndi mitengo m'munda. Chitsanzo: chimanga ndi msangu m'munda.

Ubwino wophatikiza mbewu ndi mitengo:

- Manyowa: masamba amitengo akagwa pansi amawolerana ndikusanduka manyowa, chomwe chili chakudya cha mbewu m'munda.
- Kuteteza kukokoloka kwa nthaka: Mizu ya mitengo yimapangitsa kuti dothi likhale logwirana ndipo pamene madzi wothamanga abwera amachepa mphamvu.
- Kusunga madzi: Mitengo yimapereka mithuzi m'nthaka pa chifukwa cha ichi chinyonho sichitha chomwe ndichofunika ku mbewu m'munda kuti zikule bwino.



- d) Nkhuni/Milimo: nthambi zamitengo zitawuma kapena mtengo wutakalamba wumadulidwa ndi kugwiritsa ntchito yophikira pakhomu komaso mitengo yomweyi timakozera denga la nyumba.
- e) Kuteteza kumphepo: M'nthawi yamphepo mwachitsanza kavuluvulu, mitengo ndiyo yimateteza kuti denga lisasasuke. Mitengo imatetezanso kumunda mbewu zathu kuti zisawonongeke.
- f) Zipatso: A limiwa akubzala mitengo yazipatso zomwe amadya zina kugulitsa.




## 10. Ulimi wamadimba apakhomo/panyumba (Home Gardens)

Awa ndi madimba amene amalimidwa pamalo wozungulira nyumba ya mlimi.










Ubwino wamadimba apakhomo:

- a) Kagwiritsidwe ntchito kabwino kamalo apakhomo, m'malo mongowasiya ndikumangosesapo.
- b) Mbewu zimalandira chisamaliro chokwanira.
- c) Kututa zokolola kumakhala kosavuto.
- d) Mitengo yomwe yimapezeka pakhomo yimathandiza kutipatsa m'phweya wabwino, kuteteza kumphepo yamphamvu, mthuzi, zipatso komanso khuni zophikira panyumba.





Munda osankhidwa kuti mupange dongosolo, loyesedwe ndi makina a GPS



<b>Dzina</b>	<b>Kukula kwa minda yonse kuiphatikiza pa ekala</b>
Denise	2.28
Marita	2.55
Phillimon	1.35
Isaac	3.45
Daniel	2.26
Rosaline	1.18
Florida	1.51
Chief Chimbayi	1.47
Maseko	1.34
Chokani	6.00

<b>Dzina</b>	<b>Kukula kwa madimba onse kuwaphatikiza pa ekala</b>
Denise	0.35
Marita	0.1
Phillimon	0.5
Isaac	1.6
Daniel	0.3
Rosaline	0.4
Florida	0.15
Chief Chimbayi	0.5
Maseko	0.9
Chokani	0.7